

# KUDZA KWACHIWIRI

## KWA AMBUYE



Atate Athu Akumwamba, pamene ife tikubwera kwa Inu usikuuno, mu Dzina lokondeka ilo la Ambuye Yesu, ife ndife okondwa kwambiri pamene ife tikuyandikira masiku opatulika amenewa, podziwa kuti imeneyi ikuyimira nthawi yaikulu kwambiri padziko lapansi. Ndi pamene Nsembe yokwanira muzonse iyo inapangidwa, kuti ochimwa osauka otayika akhoze kumasulidwa ndi kukhala nacho chiyembekezo chachikulu ichi chimene ife tiri nacho mkati mwa zifuwa zathu usikuuno, kuti tsiku lina Iye adzabweranso. Ndipo usikuuno, pamene tikuyandikira guwa ili, kubwera kudzera pakhomopo, ndi kumva nyimbo yakale iyi, “Ife tidzakhala ndi sabata yaikulu yobwerera kwathu, zaka teni sauzande zoyambirira,” zikubweretsa mmbuyo zikumbutso za zaka zambiri zapitazo pamene ife tinakumana kuno mu kachisi chisanayambe chitsitsimutso chachikulu cha dziko lonse. Ndipo, Atate Mulungu, ife timangoyamikira malingaliro amenewo.

<sup>2</sup> Ndipo zikuwoneka zabwino mmoyo wathu kuti ife tibwerere kachiwiri usikuuno kuti tidzayambe china cha zitsitsimutso zachikale zija kumene ochimwa amafuulira chifundo, ndi pamene wobwerera mmbuyo amakonza zinthu ndi Mulungu kachiwiri. Ndipo Mzimu Woyera ndiye Munthu wamkulu mu msonkhano, Yemwe amagwira ndi kulamalira, ndi kubweretsa kwa ife Mkate wa Moyo kudzera mu Mawu. Ndipo ife tikupemphera kuti Iye azitumikira kwa ife usiku ndi usiku mu chitsitsimutso ichi, kuchiritsa odwala ndi osowa, kuyeretsa wokhulupirira aliyense, ndi kudzitengera ulemerero kuchokera ku kuyesetsa uku komwe ife tikuchita. Pakuti, Atate Mulungu, ndi kwa ulemu ndi ulemerero wa Dzina Lake kokha kuti ife tinapempha izi. Amenii.

<sup>3</sup> Uku ndi kukwaniritsa lonjezo lomwe ine ndinapanga zaka leveni zapitazo. Nthawi yayitali kubwerera kwa ilo, koma kubwereranso ku kachisi ku chitsitsimutso. Ndipo, tsopano, ife tikudziwa kuti kachisi wathu wamng’ono ndi wosakwanira malo a chitsitsimutso, koma ife tingodzazana muno, ndipo chopambana chimene ife tingakhoze, kwa mausiku angapo otsatirawa, kwa ulemerero wa Mulungu.

<sup>4</sup> Ndipo ine ndimakonda kukhala ndi msonkhano mu tchalitchi. Malo ambiri, ife timakhala nayo iyo mmabwalo amasewera, ndi kunja, ndi mmabwalo, koma pamakhala chinachake chosiyana pamene inu mukhala nawo iwo mu

tchalitchi. Kuti zimawoneka kuti zimakhala zokoma, chiyanjano choyandikana pamene muli mu tchalitchi. Kunja mmabwalo amenewo, malo achidziko, ife tiri oyamikira chifukwa cha mwayi wokhala kunja uko, koma izo zimawoneka ngati kuti inu mumapeza kukhumudwitsidwa, ngati mphamvu ya chiwanda, imene inu mumayenera kuyiphwanya chitsitsimutso chisanayambe konse. Ndiyeno pamene inu mubwera mu tchalitchi, ndi malo amene Mulungu amakhala, ndi kubwera ku nyumba Yake kudzakhala ndi msonkhano.

<sup>5</sup> Ndipo tsopano ndife okondwa usikuuno kuwona zambiri mwa nkhope zakale zomwe ine ndinaziwona zaka zapitazo mu kumalizitsa kwa utumiki wanga kuno ku kachisi. Ndikuwona M'bale Graham mkati, ndi M'bale Curtis, ndi Mlongo Angie, ndi Mlongo Gertie kuno, ndi M'bale Cox ndi Mlongo Cox, ndipo, o, mai, ochuluka a inu, Mlongo Spencer ndi M'bale Spencer, ndi nonse a inu muno. Ndife okondwa kwambiri. Amayi, ndi Akazi a Slaughter, ndi m'bale chakuno, basi magulu aakulu a inu, apobe. Ndi angati ali muno kuyambira nthawi yomwe ife tinayamba mmbuyomo, ine ndikutanthauza pamene ine ndinachoka mu chitsitsimutso kuti ndipite kunjja? Tiyeni tiwone manja anu. Mu mpingo wonse usikuuno, tangoyang'anani pa manjawa. Ndizo zabwino kwambiri.

<sup>6</sup> Tsopano ife tiri. . . tikudziwa kuti zitsitsimutso zimadza kokha mwa Mzimu Woyera. Iye ndi Mmodzi Yemwe amabweretsa chitsitsimutso. Ndipo ife sitingakhoze kuchita izo tokha, ife tingakhoze kokha kupanga kuyesetsa kumeneko; ndipo Mulungu ayenera kudalitsa kuyesetsa kumeneko, ndipo ife tikudalira kuti Iye atero.

<sup>7</sup> Ine ndinali kumuuzza mkazi wanga pa msewu tikutsika. . . Ine sindinapeze ngakhale mwayi woti ndidye chakudya chamadzulo usikuuno. Kunali zotangwanitsa zambiri. Iyo inali 2 koloko dzulo masana ndisanavale malaya anga, kuyambira nthawi yomwe ine ndinadzuka dzulo m'mawa. Ndilo gawo la telefoni. Ndipo iyo inali pomwe pa thuu koloko pamene ine ndinali ndi zadzidzidzi kwa Dr. Sam Adair mu Louisville. Ndipo pamene. . . Ndiyeno mafoni ena ambiri, ndi amkhala kale. Imodzi inali yochokera ku chipatala, anati, "Chabwino, ife tadikirira nthawi ndi nthawi, ndipo ngati gehena ali woyipitsitsa pamene ife tidzafike kumeneko kuposa momwe masautso awa akhala ali, kudikirira." Ndipo basi kufuula ndi kulira kuchokera kulikonse, mahandiredi a atumiki.

<sup>8</sup> Ndipo, ine ndikukuuzani inu, ife tikukhala mu limodzi la masiku aakulu kwambiri amene dziko lino linayamba lawadziwapo, imodzi mwa nthawi zazikulu kwambiri. Ndipo ndine wokondwa kwambiri kuwona njala mmitima ya anthu yofuna zochuluka za Mulungu.

<sup>9</sup> Tsopano ine ndazitengera pa mtima wanga, kupemphera

kuti izo zikhale mu chifuniro cha Mulungu. Ndipo, ndisanayiwale, pali anthu ena ayimirira kumbuyo uko. Ine ndikudabwa. . . Ife tiri ndi a—mpando kuno, benchi yaing’ono, ine ndikudabwa ngati mwanjira ina ife sitingakhoze kukonza benchi yaying’ono. Ena mwa madona. . . kapena chinachake, ayima kumbuyo uko, kuti mwinamwake ife tikhoza. . . Kuno, ndikudabwa ngati ena a iwo kuno kapena chinachake, angoyenda ndi kudzakhala pa benchi pamwamba pano, pamwamba kuno kutsogolo. Mwina. . . M’bale Ben, ndife okondwa kukuwonani inu muno, nthawi yotsiriza yomwe ine ndinakuwonani inu ine ndinali ku San Fernando Valley, California, masabata angapo apitawo. Ndipo kuno kuli malo pamwamba apa ngati mukusamala kuti mubwere, inu—inu anthu kumbuyoko amene mwaima. Ndipo tsopano ngati inu mukufuna kuti mubwere apo, bwanji, bwerani patsogolo kumene. Pano pali mpando owonjezera pa nsanja pano, ndi malo ena owonjezera apa, ndipo iwo adzatengedwa pa guwa. Ife tikufuna inu mukhale omasuka momwe inu mungathere.

<sup>10</sup> Ndipo ine ndinamuza mkazi wanga kuti ine ndinadzilonjeza ndekha kuti mwa thandizo la Mulungu, ine sindikulinga kuti ndidzitalikitsa misonkhano, ndikufuna kuti ndiyankhule maminiti sate, Ambuye akalola. Ndipo chimenecho chidzakhala chozizwitsa mwa icho chokha, chifukwa ine—ine basi sindimatha kungoyamba mwachangu. Ndipo, koma ine—ine ndikungoyenera kuyesera, ndipo chifukwa cha. . . Ndipo kenako nthawi ikudza yomwe ife tiri, ino, mawa usiku. . .

Usikuuno, phunziro langa ndi: *Kudza Kwachiwiri Kwa Ambuye.*

<sup>11</sup> Ndipo mawa usiku ndi usiku wa mgonero, ndipo ine ndikufuna kuti ndidzayankhule za *Mgonero* kuchokera pamayimidwe a Chipangano Chakale. Ndipo ife tiri. . . Mawa usiku ndi usiku wa mgonero wovomerezeka, chifukwa ndi usiku umene Ambuye wathu anaperekedwa. Ndipo ndi usiku wa mgonero wovomerezeka. Ndipo ikatha misonkhano mawa usiku, utumiki wa kulalikira wachizolowezi, ndiye ife tidzakhala ndi mgonero. Ndipo aliyense akuitanidwa kuti abwere ndi ife ndi—ndi kudzatenga nawo mbali mu nkhanayi yosiyidwa ndi Ambuye wathu Yesu kwa ife.

<sup>12</sup> Ndipo kenako usiku wotsatira, Ambuye akalola, pokhala usiku wa kupachikidwa, Ndikufuna kuti—kuti ndidzatenge, kuchokera ku lingaliro losiyana mwina kuchokera pa zomwe mudzakhala mukuzimva pa wailesi, *Kupachikidwa.*

Ndipo kenako Loweruka usiku, *Kuikidwa mmanda.*

<sup>13</sup> Lamlungu m’mawa pa 6 koloko, msonkhano wa kutuluka kwa dzuwa. Pa teni koloko, utumiki wa ubatizo, ndipo ngati alipo iwo oti abatizidwe. Ndipo kenako uthenga wa mmawa wa Isitara.

<sup>14</sup> Ndipo Lamlungu usiku, Ambuye akalola, ife tikuyembekezera uthenga waufupi pa *Umboni wa Chiwukitsiro*, ndi msonkhano wa machiritso. Misonkhano ya machiritso yachizolowezi yonga timakhala nayo mu msonkhano uko mu—msonkhano wachizolowezi, pa Lamlungu likubwerali usiku. Ndipo ngati inu simunachiwonepo icho, ndipo abwenzi anu sanawonepo umboni wowoneka wa Yesu woukitsidwayo, Ine ndikuyembekeza kuti Iye adzachita monga Iye anachitira mu zaka zapitazo mmisonkhano, kuwonekera pomwe pano ndi kuchita zinthu zomwezo zomwe Iye anazichita pamene Iye anali pano pa dziko lapansi. Ndipo ife tikuyembekezera nthawi imeneyo, ikudza . . . imene ikudzayo.

<sup>15</sup> Ndiko kulondola, sunthirani mmwamba ndipo mudzadzipange nokha kumasuka monga momwe mungathere. Ndipo ine ndikudabwa ngati mwina mawa usiku tingadzakhoze kudzatenga mipando kwinakwake. Mwina kumusi ku—nyumba yokonzera maliro kapena kwinakwake komwe tingadzapeze ina yowonjezera, mwinamwake kuti idzakhale mozungulira mmbali. Ife tikufuna aliyense adzakhale womasuka momwe angathere.

<sup>16</sup> Ndi angati amawakonda Ambuye ndi zonse zomwe zili mkati mwanu? Tsopano tiyeni tingoyika zokonda zathu kwa Khristu ndipo tingoyang'ana tsopano. Ife sitiri pano chifukwa cha ziphunzitsa, ife tiri pano kuti tidzamupembedze Ambuye. Ndipo ife tiri pano kuti tiitane aliyense wa kachikhulupiriro kalikonse, mtundu, mtundu, izo ziribe kanthu kuno, ife tikungobwera muno kuti tidzamupembedze Ambuye, ndipo padzakhala theka la ora la kuyimba kwachikale ndipo—ndipo misonkhano isanayambe. Ndipo, tsopano, mawa usiku ine ndiyesera kuti ndidzayambe monga ngati usikuuno, ndendende, ngati nkotheka, pa eyiti koloko, ndi kudzatuluka mwamsanga momwe ife tingathere kuti ife tidzakhoze kubwerera usiku wotsatira.

<sup>17</sup> Ndipo, tsopano, aliyense walandiridwa. Ndipo, alendo athu, ndinu olandiridwa kuti mubwere ku chiyanjano ndipo mwamsanga msonkhano ukangotha, inu anthu apa tchalitchi kuno amene mumabwera kuno, muwonetsetse kuti inu mwamugwira chanza aliyense yemwe inu mungakhoze kutero. Basi ingokhalani . . . Basi mungosiya zigwirirozo tsopano, ndipo mungokhala ndi nthawi yodabwitsa. Ndipo inu simukudziwa zomwe Ambuye wathu angathe kuchita, ino ndi nthawi ya Isitala ndipo ife tikungoyembekezera zinthu zazikulu.

<sup>18</sup> Tsopano, mu Mawu odala, ine ndikukhumba kuti ndiwerenge basi—ndime, kapena mzere kapena ziwiri, kuchokera mu Uthenga Wabwino wa Luka Woyera, ndi mutu wa 15, ndime ya 8:

*Kapena mkazi wanji ali nazo zidutsa khumi*

*za siliva, ngati iye adzataya chidutswa chimodzi, samayatsa nyali, ndipo amasesa mnyumba, ndi kufunafuna mosamalitsa mpaka iye atachipeza icho?*

*Ndipo pamene iye wachipeza icho, iye amaitana abwenzi ake ndi anansi ake pamodzi, nanena, Kondwerani ndi ine; pakuti ine ndachipeza chidutswa chimene ine ndinachitaya.*

19 Tsopano, ilo likhoza kuwoneka ngati Lemba losamvetsaka kwambiri la Kudza Kwachiwiri kwa Khristu, ndipo...koma izo zikuyankhula za Kudza Kwachiwiri kwa Khristu. Ndipo phunziro lalikulu ili lomwe ife tiri nalo pano patsogolo pathu tsopano ndi limodzi la mitu yofunika kwambiri mu Malemba Opatulika onse. Palibe chinthu chofunika kwambiri monga Kudza kwa Ambuye Yesu. Pakuti ngati Iye sabwera, ife tapezedwa mboni zonama, akufa athu omwe ali m'manda atayika, ndipo palibe chiyembekezo chomwe chatsala kwa ife ngati Yesu sabwera mowonekera kachiwiri. Ndipo momwemo...kuwala uku, mu kuwala komweko kwa Kudza Kwachiwiri, kunali kofunika kwambiri, kuti sabata yopatulika iyi yomwe ife tikuyandikira, kuti Yesu, pamene Iye anali kuyandikira iyo nthawi yoyamba mu mithunzi ya Mtanda, Iye anayankhula zochepe kwambiri za imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro. Iye anayankhula zochuluka pa Kudza Kwake Kwachiwiri kuposa momwe Iye anachitira pa imfa Yake, kuikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro. Koteru poganizira za zimenezi, ilo liyenera kukhala phunziro lofunikira kwambiri.

20 Mu Chipangano Chakale, nthawi zambiri muli Malemba ochuluka mu Chipangano Chakale okhudzana ndi Kudza Kwachiwiri kwa Khristu kuposa momwe zinaliri ku Kudza koyamba kwa Khristu. Chirichonse kwa mtundu wa anthu, tsopano chitetezero chitatha kupangidwa, chikukhazikika mwaulemu pa Kudza Kwachiwiri kwa Ambuye.

21 Tsopano, ife tiri ndi zipembezozo zosiyanasiyana, ndipo ife tiri ndi zolinga zosiyanasiyana ndi zamulungu zosiyanasiyana, koma chipembezozo chathu cha Chikhristu chakhazikika mwaulemu pa imfa, kuikidwa mmanda, ndi chiwukitsiro, ndi Kudza Kwachiwiri kwa Ambuye. O, ndi funso lofunikira. Ndipo pamene ife tsopano tikuyandikira, ku maganizo anga odzipereka kwambiri, ife tikukhala mu mithunzi yomwe ya Kudza Kwake Kwachiwiri. Kumeneko, ku njira yanga yowonera izo mwa kuwala kwa Lemba, palibe chiyembekezo chimodzi chatsalira kwa Mpingo kunjira kwa Kudza Kwachiwiri kwa Ambuye. Dziko lapansi mu chikhaliidwe chake chakuthengo lafika kwathunthu posalamuliridwa, kwa bungwe lirilonse lopangidwa ndi anthu mu dziko. Mafumu sakukhoza kuwalamulira anthu awo konse, ngakhale olamulira mwankhanza sakukhozanso kuwalamulira, demokalase siikukhozanso kuwalamulira ake

konse, ndipo palibe chiyembekezo chimene chatsalira koma Kudza Kwachiwiri kwa Ambuye Yesu.

<sup>22</sup> Ndipo tsopano ndi imodzi mwa nthawi zowopsya kwambiri kwa wosakhulupirira ndi wochimwa, yomwe iye anayamba wachitirapo umboni, chifukwa nthawi yachiwonongeko yayandikira pafupi. Ndipo ndiyo nthawi yodalitsika kwambiri kwa wokhulupirira, pakuti chiwombolo chake chayandikira. Pali magulu awiri pa dziko lapansi usikuuno, wokhulupirira ndi wosakhulupirira. Iye amene Ambuye akubwera kudzamulandira, ndi amene Ambuye akubwera kudzamutsutsa. Pa Kudza Kwake, adzadalitsa mmodzi ndipo adzatemberera winayo, pa kuwonekera Kwake.

<sup>23</sup> Ndipo popeza kuti ichi ndi chinthu chofunikira kwambiri, ine ndikuganiza basi ndisanati... madzulo, kani, a chitsitsimutso chathu chaching'ono, kuti ife tiyang'ane mwaulemu, ndiponso tilowe m'Malemba, ndi kuwona momwe ife tiriri pafupi. Ngati ine ndikanafuna kudziwa ndi nthawi yanji iyo inali, ine ndikanayang'ana pa wotchi yanga. Ngati ine ndikanafuna kudziwa ndi tsiku lanji la sabata lomwe ife tinali kukhalamo, kapena mwezi wa pachaka, ine ndingayang'ane pa kalendala. Ndipo ngati ine ndikufuna kudziwa nthawi ya kuyandikira kwa chochitika chachikulu ichi, Ine ndimayang'ana pa Mawu a Mulungu, Iwo amanena za nthawi pamene icho chiri pafupi. Pakuti Baibulo linati, "Pamene zinthu izi zidzayamba kuchitika, mudzatukule mutu wanu, chiwombolo chanu chayandikira." Nthawiyo yayandikira.

<sup>24</sup> Icho chinali chinthu chachikulu chotero kwa Yohane, mvumbulutsi, pa Chisumbu cha Patmo, kuti pamene iye anawona chiwonetsero cha Kudza kwa Ambuye. Pamene iye anawona matemberero amene anali pa wosakhulupirira, ndi madalitso amene ali pa wokhulupirira, iye anafuula, "Ngakhale choncho, bwerani, Ambuye Yesu!" Izo zinamusangalatsa mtima wake pambuyo pa zonse zomwe iye anaziwona, zochitika Kubwera Kwake kusanachitike, iye anafuula, "Ngakhale choncho, bwerani, Ambuye Yesu!" Ndipo pamene m'badwo wonse wa mpingo unali utadutsa mu kuwona kwake, ndipo iye anawona chirichonse mwathunthu, momwe izo zikanadzachitikira, ndiye anafuula, "Bwerani, Ambuye Yesu!" Icho chiyenera kukhala chinthu chaulemerero kuti Kudza kwa Ambuye kwayandikira pafupi.

<sup>25</sup> Yesu, pamene ophunzira Ake anafika pa malo pamene iwo anali kuyang'ana pa zachithupithupi kapena zinthu zachilengedwe za padziko lapansi. Tsopano, apa ife tikufuna kuti tiyime maminiti pang'ono chabe. Sikuti nthawi zonse zimakhala zachithupithupi zomwe zingatikokere ife kutali, nthawizina zinthu zachilengedwe zokha zimatikokera ife kutali. Atumiki a Yesu, kapena ophunzira Ake, anali kulozera kwa Iye kachisi wa mzinda, Yerusalemu, kachisi wamkulu kumene

Mulungu mu Ulemerero Wake wa Shekina anali atawonekera m'Malo Opatulikitsa a Opatulika. Ndipo pamene iwo anamuuza Iye za ubwino wa momwe miyalayo inaikidwira, momwe wolamulira wamkulu wa Mulungu anakonzeratu kuti miyala iyi idulidwe mmalo ambiri mu dziko lapansi ndi kubwera pamodzi. Ndipo mu zaka forte za kumangidwa kwake, panalibe ngakhale phokoso la macheka kapena phokoso la nyundo. Izo zinayikidwa mwaluso pamodzi. Ndi kuti momwe Mulungu anadzera pamwamba pa Akerubi ndipo izo zinawonetsera Ulemerero Wake wa Shekina, ndi momwe iwo anali ndi chiyembekezo chachikulu mu mpingo waukulu uwu.

<sup>26</sup> Ndipo Yesu anati kwa iwo, “Musawone zinthu zonse izi.” Komabe iwo anali malo oyera, iwo anali malo abwino. Iwo anali malo, nyumba yokhalamo ya Ambuye. Koma Yesu anati, “Musati muziwona zinthu izi. Ine ndiri ndi chinachake choti ndikuuzeni inu chimene chiri chachikulu kuposa ichi. Pakuti pakudza nthawi,” Iye anati, “kuti sipadzasiyidwa mwala umodzi pa umzake.”

<sup>27</sup> Ziribe kanthu mwabwino bwanji momwe ife timayesera kusamalira thupi lathu, ziribe kanthu ndi molimbikira bwanji momwe ife tingagwirire ntchito kwa bungwe lathu, ndi molimbika bwanji momwe ife timagwirira ntchito mu mpingo kwa lathu—dongosolo lathu la mpingo, ikudza nthawi pamene zinthu zonse izo zidzachoka ndi kupita.

Yesu anayamba kuwauza iwo zimenezo, ndipo iwo anati, “Kodi chizindikiro cha kubwera kwa mapeto a dziko chidzakhala chiyani?”

<sup>28</sup> Ndipo Yesu anayamba kuyankhula kwa iwo, “Nthawi idzafika pamene sipadzakhala mwala utasiyidwa pamwamba pa umzake. Inu mudzamva za nkondo ndi mbiri za nkondo, miliri, zivomezi m'malo osiyanasiyana.”

<sup>29</sup> Ndipo tsiku lina, uko ku California, uko mu Oakland, pamene iwo unali mwayi wathu woti tikhale kumeneko mu msonkhano, ndipo iyo inali nthawi yoyamba imene mkazi wanga anayamba wakhalapo mu chivomezi. Ine ndinali nditakhala mmalo ometa, ndipo ine...chipindacho chinagwedezeka pang'ono pokha. Ndipo wailesi inalengeza mwachangu, “Chivomezi chikuchitika.” Anati, “Iwo akuyembekezera china mkati mwa maminiti eyiti.”

Ndipo ine ndinaganiza, “O, bwanji ngati ichi chiri chomaliza!”

<sup>30</sup> Ine ndinatuluka mwachangu kuchokera pa malo ometa, ndinakumana ndi mkazi wanga yemwe anali kundidikirira pa msewu, ndinalowa mu kasitolo kakang'ono ka mankhwala kuti ndikapeze makadi a zithunzi kuti tikatumize kwa okonedwa athu. Ndipo pamene ife tinali kumeneko, chimodzi mwa zinthu zachinsinsi, kumverera kwachilendo komwe munthu

angakhonze kukumverera, dziko lonse lapansi linayamba kugwedezeka. Mabotolo anayamba kugwa kuchokera pa alumali, zotulutsira utsi zinayamba kugwa pa nyumbayo, ndipo mu msewu, mukuyenderera, anthu akufuula ndi kulira pamene pulasitala inkagwa kuchokera pa makoma. Ndipo nyumba zazikulu zokhala ndi magawo sate ndi forte, zinagwedezeka pamodzi mpaka utsi kapena fumbi lochokera mu mtondo linakwera ngati bowa wamkulu. Ndipo anthu anayamba kufuula ndi kumathamanga. Ine ndinati, “Chimenecho ndi chala cha Mulungu Wamphamvuzonse, chikuti, ‘Cholembedwa chiri pa khoma.’”

<sup>31</sup> Yesu anati, “Pamene inu mudzamva za zivomezi m’ malo osiyanasiyana.” Nthaka inang’ambika mu msewu waukulu kwa mtunda wautali, pafupifupi mapazi asanu, ndipo zinapita pansi kutali mapazi mahandiredi mu nthaka. Malo amodzi, msewu waukulu wonse unagwera mkati. Ndipo ine ndinaganiza pamene iyo inang’ambika, ine ndinangotsala pang’ono kuwona chala cha Mulungu Wamphamvuzonse, chikuti, “Ndipo kudzakhala zivomezi m’ malo osiyanasiyana.”

<sup>32</sup> Pamene tsiku linali kupitirira, zivomezi eyiti zosiyanasiyana zinagwedezeka mzinda umenewo. Ndipo malo omwera mowa anakhala chitsegulire, ndipo zidakwa zinakhamakira mmisewu. Ndipo akazi ankayenda mmisewu, atavala mwatheka, ndi chirichonse ngati kuti palibe nkomwe chimene chinali chitachitika. Anthu ali omangirizika kudziko lapansi lero mpaka ine sindikudziwa chomwe chingatengere kuti ndigwedezeka dziko lino. Iwo amangowoneka kuti ali osakhudzidwa kwenikweni. Iwo samazindikira. Ndipo munthu wina anapanga ngakhale ndemanga, monga ine ndinamumva iye ndi diso langa, anati, “Kodi inu munawona zomwe ine ndinachita? Ine ndinagwedezeka chibakera changa. Ine ndine munthu wamphamvu.”

Ndipo ine ndinaganiza, “Mwano wotero!”

<sup>33</sup> Ine sindinaganizepo zochuluka za izo ngati mwano monga momwe ine ndinachitira kuno mumzinda wathu womwe, pamene ine ndimatuluka mumsewu waukulu usiku watha kupita ku Georgetown, pamene mukuwoloka malire kunjika kuno basi musanafike mu msewu wawukulu watsopano pamene ukulowera. Pamenepo panali chikwangwani chachikulu chitakwezedwa mmwamba pamenepo, ndipo icho chinati, “Iye wawuka, ali nawo Moyo.” Ndipo chikwangwani chotsatira chomwe, izo ziwiri zokha, zinati, “Kumene kuli mowa wa Budweiser, kuli moyo.”

<sup>34</sup> Ine ndinaganiza, “Mwano wotero!” Ndizo zonse zomwe zilipo kwa izo. Ndipo Baibulo linanena kuti, “Kusanafike Kudza Kwachiwiri kwa Khristu, kuti anthu ayenera kudzakhala amwano, akuyenda mu zisiriro za iwo eni zopanda umulungu,



ophwanya malamulo, ndi onenera zonama.” Momwe dziko lakhalira mu chinyengo chotero!

<sup>35</sup> Mu Bombay, India, posachedwapa pamene Billy (mnyamata wanga) ndi ine tinali kumeneko mu msonkhano waukulu kumene ma teni a masauzande a ma Hindu anapereka moyo wawo kwa Khristu, apo panadza chenjezo lalikulu. Ndipo ine ndikufuna inu kuti muwone luntha la chilengedwe. Ndipo, zonse mwadzidzidzi, mwa chifukwa china chosadziwika, mbalame zazing’ono zonse mu mzindawu zinayamba kunyamuka kuchoka mdzikomo. Ndipo mbalame, mwa unyinji zinachoka mdzikomo. Ndipo iwo anayamba kuzindikira ng’ombe zonse ndi nkhosa ndi ng’ombe za pagoli. Koma mu India, mipanda yawo siili ngati mpanda wathu, iyo simakhala mipanda yamatabwa, iyo ndi mipanda yayikulu yamiyala yomwe imamangidwa motalika. Ndipo ng’ombe zonse zinayamba kuchoka pa pakoma ndi kuchoka ku nyumba, ndi kupita kutali pakati pa munda ndi kuyamba kusonkhana mozungulira pakati pa munda. Kenako, zonse mwadzidzidzi, chivomezi chachikulu chinakantha ndi kugwetsa makoma, mitengo, miyala, mizinga inawuluka. Ndipo mbalame sizinabwerere, ndipo ng’ombe zinakhala mmunda, ndipo munthu anapita motsatira akuganiza kuti izo zinali zonse zabwino. Ndipo tsiku lotsatira, chivomezi china chinagwedeza, ndipo nyumba zambiri zinatembenezika ndipo mizinga inawuluka. Ndipo pa tsiku lachitatu, ng’ombe zinabwerera ku mpanda ndipo mbalame zinabwerera ku mzindawo.

<sup>36</sup> O, Iye Amene amadyetsa mpheta, Iye amene anabweretsa zolengedwa Zake zazing’ono mu chombo, akadali moyo ndipo akulamulira. Ndipo izo zimawoneka kuti ziri ndi luntha lochuluka pa za Mulungu kuposa mmene munthu amachitira, amene Iye anamulenga mu chifanizo Chake; pamene, munthu amachitira mwano. Zolengedwa zazing’ono za dziko lapansi, Mulungu amazisamalira izo ndipo izo zinapanga njira yawo kuchoka pa makoma aakuluwo. Izo zikanakhala zitaphedwa, mbalamezo zikanakhala zitaphwanyidwa mming’alu ya miyala pamene iyo inkagwedezeka uku ndi uku.

<sup>37</sup> Zizindikiro za Kudza Kwake! O, ndi tsiku lalikulu lomwe ife tikukhalamo tsopano. Zivomezi mmalo osiyanasiyana, miliri, zinthu zonse izo zimene Yesu anazinena ziri pano. Mwa njira yanga yowonera izo, ine sindikuwona chirichonse chitatsalira koma Kudza kwa Ambuye. Iko kuli pafupi.

<sup>38</sup> Yesu mu...ndiponso mmawu Ake kwa anthu Ake, Iye anati, “Phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu. Pamene iwo uli wanthete ndi kuyamba kuphuka masamba, inu mumati dzinja layandikira. Ndipo pamene inu muwona zinthu izi zikuyamba kuchitika, zindikirani kuti nthawiyo yayandikira.”

<sup>39</sup> Zindikirani chomwe mtengo wa mkuyu unali. Mtengo wa

mkuyu nthawi zonse wakhala uli fuko la Ayuda. Iye sananene kokha “mtengo wa mkuyu,” koma “mitengo ina.” “Pamene inu muwona mtengo wa mkuyu ndi mitengo ina yonse ikutulutsa mphukira.” Tsopano, Iye anayankhula osati za mtengo wa mkuyu wokha, komanso mitengo *ina*.

<sup>40</sup> Tsopano, tiyeni tingozindikira pamene iwo ukutulutsa mphukira yake. Ife takhala mu nthawi yachilendo kwambiri mu zaka zingapo zapitazi. Mpingo wa Amitundu wakhala nacho chimodzi cha zitsitsimutso zazikulu kwambiri chimene iwo wakhalapo nacho chiyambireni kumeneko...kuyambira masiku a atumwi; o, ndipo mpingo wa Amitundu unalibe chitsitsimutso pamenepo, iwo unali mpingo wa Chiyuda umene unali ndi chitsitsimutso. Koma mpingo wa Amitundu, mu zaka teni kapena thwelofu zapitazi, wakhala uli ndi chitsitsimutso chachikulu cha mbiriyakale.

<sup>41</sup> Ife tikuganiza za chitsitsimutso cha Martin Luther, inde, bwana, icho chinali chachikulu, koma icho chinali mu Germany mokha. Ife tikuganiza za chitsitsimutso cha Wesile chomwe chinali ku England, icho chinafalikira cha kuno, ndi zisumbu zingapo za Britian, koma sichinatenge mphamvu kwambiri. Koma mu tsiku lino, chitsitsimutso ichi chimene chilipo, cha Chazimu, mwamtheradi chakwanira kuchokera ku nyanja kupita ku nyanja yopanda malire, padziko lonse lapansi, kudzera mu wailesi ndi magazini ndi alaliki omwe atuluka kunja, osathandizidwa ndi mtundu wa anthu, ndipo abweretsa chitsitsimutso mwakuti masauzande a zikwi kuchulukitsa zikwi (a miyoyo) yabadwa mu Ufumu wa Mulungu.

<sup>42</sup> Mu utumiki wanga womwe wofooka womwe Ambuye wandipatsa ine, Ndawonapo anthu oposa miliyoni imodzi akubwera ku Ufumu wa Mulungu. Taganizirani za izo! Pamene ena ndi mautumiki aakulu awa, omwe amasesa pa wailesi, ndi zina zotero, kwa mamilioni. Pali moto wa chitsitsimutso umene wayatsidwa pa phiri lirilonse mu dziko lapansi, kwenikweni, kuyambira ine...kuyambira zaka teni zapitazo, kuyambira ine...ife tinayamba mu chitsitsimutso. Ife tiri pa nthawi yotsiriza.

<sup>43</sup> Tsopano zindikirani, ndiye, basi izo zisanachitike, Iye analosera apa, ndipo anati, “Makoma a Yerusalemu adzaponderezedwa pansu ndi Amitundu mpaka nyengo ya Amitundu itatha.” Achimuhamedi awulanda iwo. Ife tikuzindikira zimenezo. Ndipo ine ndikufuna kuti inu muyang’ane pa vutoli usikuuno, momwe Ishmaeli ndi Isaki akadali pakhosi pa wina ndi mzake, ku Yerusalemu komwe kumene zinanenedweratu kuti iwo akanadzakhala. Ndipo zaka zingapo zapitazo kunalibe Ayuda aliwonse mu Yerusalemu.

<sup>44</sup> Tsopano, Yesu akuyankhula, “Pamene inu muwona mtengo wa mkuyu ukuphuka masamba ake.” Tsopano,

Ayuda amwazikana ku dziko lonse lapansi, chiwerengero chachikulu, mamiliyoni mu Germany, ndi mu Italy, ndi mu United States, ndi padziko lonse lapansi. Ndipo Mulungu, monga Iye anachitira mmasiku oyambirira, anawumitsa mtima wa Farao, Iye anawumitsa mtima wa Mussolini pa Ayuda, ndipo Ayuda anathamangitsidwa ku Italy. Iye anawumitsa mtima wa Hitler, ndipo iwo anathamangitsidwa ku Germany. Iye anawumitsa mtima wa Stalin, ndipo iwo anathamangitsidwa ku Russia.

<sup>45</sup> Ndipo kodi inu mwakhala mukuzindikira pepalalo, kuti ife, a United States, tikutenga mbali ndi Aluya? O, m'bale, cholembedwa chiri pa khoma! Mulungu anati, "Aliyense amene adzadalitsa Israeli adzadalitsidwa, amene atemberera Israeli adzakhala wotembereredwa."

<sup>46</sup> Tsopano, ine ndiri ndi chithunzi kunyumba, kapena ine ndikukhulupirira icho chinabwerekedwa pa nthawiyo, chotchedwa ndi asayansi, *Maminiti Atatu Pasanafike Pakati pa Usiku*. Ngati dziko lasayansi lanena "kolokoyo inazungulira mpaka mphindi zitanu pasanafike pakati pausiku," ndipo ine ndikuganiza iwo adula icho tsopano mpaka pafupifupi miniti imodzi pasanafike pakati pausiku, pamene iwo anapeza haidrojeni kapena okosijeni, atomiki, ndi mphamvu zonse zazikulu izo zomwe iwo akanakhoza kuzigwiritsa ntchito, akhoza kuwononga kwathunthu mu mphindi faifi. Iwo akanakhoza, mwamtheradi usikuuno, osakhalapo munthu mmodzi wamoyo mu kontinenti yonse ya North America mu maminiti sate. Ndipo icho chagona mu gulu la anthu achikunja omwe amadana nafe. Ndipo, pambali pa izo, ife tiri ndi ngalawa ndi zombo zokonzekeretsedwa, zonse zitayikidwa mozungulira, pa zonse ziwiri. . . kudutsa Siberia, uko mu Hungary, ndi malo osiyanasiyana, kumene zombo zathu ziri, zitadzazidwa ndi mtundu womwewo wa mizinga.

<sup>47</sup> Abale, ndi mochedwa kuposa momwe inu mukuganizira! Sodomu ndi Gomora sankadziwa, usiku umenewo, kuti iwo anali kukhala moyo ora lawo lotsiriza. Igupto sankadziwa kuti mngelo wa imfa, yemwe anali atalosedwa kuti adzabwera, akanadzabwera usiku umenewo. Pearl Harbor sanazindikire kuwukira kumeneko komwe kunachitika. Ife tayedwa pa muyezo ndipo tapezeka kuti ndife operewera! Ife tayandikira nthawi yakumapeto!

<sup>48</sup> Chingachitike ndi chiyani ngati...? Iwo, komwe ku Moscow, akanakhoza kulondolera mizinga, motsogozedwa ndi nyenyezi ndi radar, akanakhoza kuponyera bomba limenero ndendende pa Fourth Street mu Louisville ngati iwo akanafuna kuteru. Uko nkulondola. Ndipo ife tingakhoze kuyima kunja uko mu nyanja kwinakwake, pa zombo zathu, ndi kulondolera umodzi molunjika ku likulu la Moscow ngati ife tikufuna kuteru. Chingachitike ndi chiyani, m'bale wanga,

ngati kutembenuka kwa mzinga kwakukuluko kungachitike ndipo dziko lino likanagwedezeka, pa ora lomwelo ife tingasiye zinthu zomwezo ndi kuzimenyetsa izo ku mbali inayo? Ndipo ife tikukhala pa kachidutswa kakang'ono, kochepa, kopyapyala kowonda, mulimonse, pamene zivomezi zadya mozungulira ndi kudya mozungulira mpaka ziri ngati kubowola dzira. Ngati iye angapangitse kuphulika kumodzi kwakukulu ndipo chiphalaphala chotalika mailosi eyiti sauzande ichi chingatumphukire m'mlengalenga, izo zikanadzachita chimodzimodzi zomwe Mulungu ananena kuti zikanadzachitika.

<sup>49</sup> Ife tiri pa nthawi yotsiriza, ife tiri pano. Palibe njira yoletsera izo. Kupempha konse...Ife tikhoza kuyika Eisenhower mu chigawo chirichonse, ndipo izo sizidzayimitsa konse izo. Yesu Khristu anati nthawi izi zidzafika, ife tiri pano. Mtengo wa mkuyu ukutulutsa mphukira yake.

<sup>50</sup> Mu chithunzi ichi, kutali komwe ku Iran, inu munawerenga mu magazini ya *Look*, momwe kuti iwo anatenga ndege zikuluzikulu ndi kupita kumeneko ndipo anakatenga ndege zodzaza ndi Ayuda awa. Masauzande a iwo, akhala ali kumeneko kuyambira pa kuthetsedwa kwa Babeloni, akhala ali mmenemo kwa zaka twente faifi handiredi, ndipo anali atasiyidwa kumusi uko. Iwo anali kulima ndi zida zakale zamatabwa. Iwo sankadziwa kanthu za Yesu kukhala konse pa dziko lapansi. Iwo sankadziwa kanthu za chirichonse koma miyambo yawo yakale ya Chiyuda, miyambo imene iwo ankakhaliramo. Ndipo pamene ndege izi zinatera pansu, ndi kuyamba kuwalongedza Ayuda awa, kuti ziwatengere iwo kubwerera ku dziko la kwawo. . .

<sup>51</sup> Mneneri analosera, zaka twente eyiti kapena sate handiredi zapitazo, ndipo anati, "Pamene iwo adzatuluka mu ukapolo umenewo, Mulungu adzawabweretsa iwo pa mapiko a mphungu." Mneneriyo anawona ndege ikubwera, iye anaziwona izo zitatera pansu, ndi kumawanyamula iwo ndi kumawatengera kubwerera ku dziko la kwawo. Iye sankadziwa choti ayitche iyo, iye basi. . .Inkawoneka ngati mphungu kwa iye, kotero iye anati, "Iwo adzabwezeretsedwa pa mapiko a mphungu."

<sup>52</sup> Ndipo pamene iwo anatuluka mu ndegemo, ndipo aang'ono anali kuthandiza okalamba, iwo ankafunsidwa. Ndipo iwo ankati, "Kodi inu mwabwerera kumodzi kuti mudzafe?"

Iwo ankati, "Ayi. Ife tabwereranso kuti tidzamuwone Mesiya!"

<sup>53</sup> O, zombo zazikulu zochokera padziko lonse lapansi, mu zaka zingapo zomalizira, zinalowa mu Yerusalemu ndi Ayuda okalamba, achichepere ndi achikulire, atavala zovala zawo, akuchokera kummawa, kuchokera kumadzulo. Ndipo yapachikika pamwamba pa likulu la Yerusalemu ndi nyenyezi yakale ya nsonga zisanu ndi imodzi ya Davide, mbendera yakale kwambiri mu dziko lapansi, siyinawuluke kwa zaka twente faifi

handiredi, lalengezedwa kukhala fuko usikuuno. Mtengo wa mkuyu ukutulutsa mphukira yake.

Yerusalemu akukula, Ambuye akubwezeretsa,  
Zizindikiro zomwe aneneri ananeneratu;  
Masiku a Amitundu akuwerengeka, ndi  
zowawitsa zochuluka;  
“Bwererani, O omwazika, kwanu komwe.”

Pakuti tsiku la chiwombolo layandikira,  
Mitima ya anthu ikulephera mwa mantha;  
Dzazidwani ndi Mzimu wa Mulungu, nyali  
zanu zikhale zokonzedwa ndi zowala,  
Yang’anani mwambwa! Chiwombolo chanu  
chayandikira.

54 Ndi mochedwa kuposa momwe ife tikuganizira. Ife sitimabwera ku tchalitchi kuti tidzakhale pa mpando, ife sitimabwera ku tchalitchi kuti tidzamve ulaliki wabwino, kapena kubwera ku tchalitchi kuti tidzamve nyimbo zabwino. Izo zonse ziri nawo malo awo, koma chimene ife kulibwino tibwere ku tchalitchi kuti tidzachite ndi kudzifufuza ndi Mulungu ndi chipulumutso cha moyo wathu, pakuti Tsiku la chiwombolo layandikira.

55 Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, anafanizira izi (Iye ananena) kwa mkazi. Ndipo mu phunziro lathu usikuuno, ife tikupeza mkazi uyu, mwamuna wake anali atachokapo, ndipo iye anali atataya chimodzi mwa zigwinjiri kuchoka pa tabuleti yake. Tsopano ine ndiyesera kuzifotokoza izo.

56 Lero, ngati mkazi ali wokwatiwa, iye ayenera kuvala mphete yaukwati ngati chizindikiro chakuti iye wakwatiwa. Ndiko kuletsa amuna ena kuti asakhale ndi chochita ndi iye. Iwo amayang’ana ndipo iwo amawona kuti iye ndi mkazi wokwatiwa.

57 M’masiku amenewo, iwo analibe mphete zaukwati, iwo anali ndi tabuleti (iwo amachitcha icho “tabuleti”) iwo amavala icho pamutu pawo. Ichu chinali ndi zigwinjiri teni, ndipo izo zinkayenda mowuzungulira mutu wawo. Ndipo icho chinali chizindikiro kuti iwo anali mkazi wokwatiwa, ndipo panalibe mwamuna amene anali woti apusitsidwe nawo iwo, panalibe anyamata oti akopeke nawo iwo. Iwo anali okwatiwa.

58 Iliyonse ya zigwinjirizo...Ngati ife tikanangokhala ndi nthawi (koma ine ndiribe, ine ndiyesera kusunga mawu anga momwe ndingathere), Ine ndikanakhoza kukuuzani inu chimene chirichonse cha zigwinjirizo chinkatanthauza. Izo zinkaikidwa mmenemo, ndipo chigwinjiri chirichonse chinkatanthauza ukoma winawake wa mkazi ameneyo. Choyamba, kutanthauza chikondi chake kwa mwamuna wake. Chachiwiri, lumbiro lake la ukoma kuti akhala moyo woyera kwa iye. Ndipo chachitatu ndi chachinayi ndi chachisanu, mpaka chanaini, ndi cha teni.

<sup>59</sup> Ngati inu mukufuna kuziyang'ana izo, yang'anani mu Agalatiya 5. Inu mudzapeza kuti mkazi ameneyo ankayimira Mpingo, ndipo Mpingo ndi Mkazi wopalidwa ubwenzi kwa Khristu. Ndipo tabuleti yomwe Mpingo ukuyenera kuti uzivala ili pa Agalatiya 5, chimene chiri chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, ubwino, chifatso, kudekha, chipiro. Imeneyo ndiyo tabuleti imene ikuyenera kuti idzivalidwa mu Mpingo, chikondi cha pa abale, chifundo, chiyanjano.

Ndipo mkazi uyu, pamene izo. . . Iko kuyenera kuti kunali pafupifupi kutada mwakuti iye anzindikira kuti anali atataya chimodzi mwa zigwinjiri zimenezo.

<sup>60</sup> O, ngati panayamba pakhalapo nthawi yomwe mpingo umayenera kuchita kafukufuku kuti mudziwe ngati muli ndi zigwinjiri zonse, iyo iyenera kukhala tsopano. Iko kukuda. Zo—zozunza zomwezo ndi mitambo yowononga chitukuko ikulendewera padziko lapansi, uchimo ndi nyansi pa mbali iliyonse. Ife tikukhala mu nthawi yopambana, pamene kuli kuipa, anthu amene amapita ku tchalitchi chifukwa cha chinyengo, anthu amene amapita ku tchalitchi kuti ayesere kubisa umbombo wawo, anthu amene amapita ku tchalitchi ndi kumadzinenera Chikhristu ndi kumakhala monga dziko lonse lapansi, kumwa, kusuta, njuga; akazi ovala mopanda makhalidwe, ovala zovala zomwe iwo samayenera kuti azivala mu—mu chipinda chawo chovalira, kunja mmisewu pamaso pa anthu. Ndipo chikondi cha pa abale ndi chinthu chimene chikupita, pafupifupi. Ife sitinataye chigwinjiri *chimodzi*, koma ife tataya kwenikweni *chilichonse* cha izo.

<sup>61</sup> Ndipo usiku unali kuyamba, ndipo, kumbukirani, mwamuna wake amatha kubwerera. Ndipo ngati iye ampeza iye ali ndi chimodzi cha zigwinjirizo palibepo, izo zinkasonyeza kuti wayikidwa chizindikiro “hule.”

<sup>62</sup> Ndipo ngati iye ananyoza, kapena, kudzidetsa yekha mwa njira iliyonse ndipo izo nkuwonedwa ndi anthu, iwo ankamubweretsa iye pamaso pa wansembe ndipo ankabweretsa mboni kuti iye anali atapezeka chomwecho, ndipo wansembeyo akawona kuti iye anali mkazi wokwatiwa, amatenga chigwinjiricho (kuchoka pa tabuleti yake) chimene iye wakhala akuchita nacho cholakwika. Ngati iye anali—anali atawononga ukoma wake, iwo amachichotsa icho. Ngati iye anali kukopa, kusonyeza kuti iye sanali woona kwa mwamuna wake, iwo amachotsapo chimenecho. Chirichonse chimene icho chinali, iwo amachichotsapo icho. Ndipo pamene mwamuna wake abwerera, iye amapeza kuti iye anali atakidwa chizindikiro, ndipo iye amatha kumusudzula iye pomwepo ndi kusakhala ndi kanthu kochita ndi mkazi wotero. Iye sanafune mkazi woteroyo.

Kotero kumayamba kuchita mdima pamene iye ankazindikira kuti anali atataya chinachake, nthawi yoti

mwamuna wake amabwera, ndipo kukuda.

<sup>63</sup> Mpingo kuli bwino uzikhala ukudzifufuza wokha ndi Mawu a Mulungu, chiyero chathu, kukhulupirika kwathu, kudzipereka kwathu. Ife tasandulika obwebweta, amiseche, osuta ndudu, a matetano, Ayezebeli odzipaka utoto, chirichonse chomwe chiri mu kalendala chomwe dziko lonse lapansi limachita, mpingo Wachikhristu ukuyanjana mu zinthu zimenezo lero mpaka inu simungakhoze konse kusiyanitsa wina kwa umzake. Ndi nthawi yoti tichite kafukufuku. Nthawi ikupita.

<sup>64</sup> Tsopano, ndi cholinga . . . kunali mochedwa kwambiri mpaka iye anayenera kuti ayatse kandulo. Ndipo iye anatenga kandulo. Sikuti iye anangotenga kokha kandulo, koma iye anatenga tsache ndipo iye anayamba kukonza m'nyumba.

<sup>65</sup> O, m'bale! Ngati panakhala kufunikira kwa nthawi ya kuyatsa kwa kandulo, kutumiza kwa Kuwala kwa Uthenga, Mzimu Woyera kubwerera mu mpingo . . . Osati mochuluka kwa zomverera, osati kwa zotengeka zina, osati kwa zomverera zina, osati kwa zodumpha chifukwa cha chimwemwe, koma chifukwa cha chochitika chofufuza mtima pamene amuna ndi akazi akhala mowona ndi Mulungu. Kulondola. Ife tiri pa nthawi yotsiriza.

<sup>66</sup> Ndipo iye anayatsa kandulo, kuti imupatse iye kuwala. Ndipo, m'bale, kandulo yaying'ono iliyonse muno iyenera kuti iyatsidwe usikuuno. Osati zokhazo, koma iye anatenga tsache, ndipo oyandikana nawo ankakhoza kuwona fumbi likuwuluka. Iye anali ndi nthawi yeniyeni yoyeretsa m'nyumba, pakuti mwamuna wake anali pafupi kubwera. Ndipo ngati iye akanamupeza iye ndi chigwinjiri chimodzi icho palibe, iye anali "hule."

<sup>67</sup> M'bale, ife Mpingo wa Mulungu wamoyo, mmaora aakulu awa amene ife tikukhalamo tsopano, izo zikutiyenereza ife kuti tidzifufuze, kupita pamaso pa Mulungu, kuyatsa kandulo ya Mawu a Uthenga, ndi kudzifufuza tokha ndi kupeza ngati ife sitikuperewera, ndipo makamaka pamene ife tiwona zinthu zonzezi zikubwera. Ife tiri pa nthawi yotsiriza, Kudza kwa Khristu kuli pafupi. Palibe chiyembekezo china padziko lapansi kwa Mpingo.

<sup>68</sup> Ndipo, penyani, mpingo ukuchita zachinyengo. Mpingo ulibenso chikumbumtima nkomwe. Inu simungathe kuwadzutsa iwo. Baibulo linati iwo adzafika mu chikhalidwe chimenecho pamene iwo azidzati, "'Tawonani, Ambuye wathu akuchedwetsa Kudza Kwake.' Ndipo iwo adzakhala akulikhwirana ndi kulumana wina ndi mzake, ndi zina zotero, ndi kumamenyana pozungulira." Ndizo ndendende basi ora limenero. Chirichonse chakonzeka. Masamba akutembenezidwa, monga izo zinaliri monga choncho, ndipo izo zakonzeka, Kudza kwa Ambuye.

<sup>69</sup> Mpingo wa Lutera unataya kuwala kwake. Mpingo wa Methodisti unataya kuwala kwake. Mpingo wa Baptisti unataya

kuwala kwake. Mpingo wa Chipentekoste unataya kuwala kwake. Kuwala kulikonse kukuwoneka kuti kwapita.

<sup>70</sup> Anthu Achipentekoste, anthu Achiyero, akuchita chimodzimidzi basi monga Amethodisti. Amethodisti akuchita monga Abaptisti. Abaptisti akuchita monga Achilutera. Achilutera akuchita monga Achikatolika. Ndipo izo zonse zabwerera ku chisakanizo chimodzi chachikulu cha tchimo. Uko nkulondola. Ife tiri mu nthawi yotsiriza, Kudza kwa Ambuye.

<sup>71</sup> Tsopano, iye anali ndi nthawi yoyeretsa m’nyumba. Iye anakwecha pansi, iye anasesa makoma, iye anagwetsera pansi akangaude, iye anapitirizabe mpaka iye anapeza chimene iye anataya. Ndipo, pamene iye anatero, iye anayitana mpingo yake yaying’ono ya paulongo kuti ibwere tsopano.

<sup>72</sup> Ine sindikusamala ngati ndinu wa Methodisti, Baptisti, Pentekoste, Presbateria, bwerani, tiyeni ife tikondwere limodzi. Pamene nthawi imeneyo ifika, pamene mpingo upeza chikondi cha pa abale, pamene mpingo upeza chiyero chake chopatulika, pamene mpingo upeza malo ake mwa Khristu, iwo udzayitanira kwa ziwalo zina za thupilo, “Bwerani ndipo mudzakondwere nafe.” Mulungu amafuna kuti mpingo udzimukonda Iye.

<sup>73</sup> Ine ndikukhulupirira linali Lamlungu mmawa pamene ine ndinali kuyankhula za ukoma wa mkazi, wodala bwanji, ndani angapeze chinthu chokoma kuposa kubwera kunyumba wotopa, pamene Mulungu wamupatsa mwamuna mkazi. Mwamuna ndi mkazi sasiyanitsidwa, iwo ali mmodzi. Mu chilengedwe, Mulungu anawalenga onse awiri pamodzi, ndipo iwo ali mtima umodzi, moyo, malingaliro, ndi chirichonse. Pamene Iye anapanga munthu mu fumbi la dziko lapansi, Iye anamulekanitsa iye kwa mkazi wake. Pamene Iye anamupanga Eva, Iye sanapite kukamupanga a—mkazi, kutenga dothi *lina*, koma Iye anatenga kuchokera ku mbali ya Adamu nthiti ndipo anapanga mkazi wake. Iye anati, “Iye ndiye fupa la fupa langa, mnofu wa mnofu wanga.” Iwo anali amodzi mu mtima, moyo, ndi thupi.

<sup>74</sup> Ndi choyimira cha Khristu. Mulungu sanawutengere Mpingo wa Khristu kuchokera ku kachikhulupiriro, ngakhalenso Iye sanawutenge Iwo kuchokera ku chipembedzo. Iye anawutenga Iwo kuchokera mu mtima wa Khristu, mkondo mu mbali Yake, kudzera mu Magazi.

<sup>75</sup> M’bale wanga, mlongo, ine sindikusamala momwe iwe ungakhalire wachipembedzo, ngati iwe sunaphimbidwe ndi Magazi, iwe watayika. Ife tilowa mu zimenezo, usiku wa mkucha, kuzasonyeza momwe izo ziliri zofunikira. Koma ndinu wotayika popanda Magazi.



Tsopano, ndiye pamene Iye anamupanga mkazi ameneyo, iye anali mzake. Chinali chinachake kwa iye choti azichikonda, chinali gawo la iye.

<sup>76</sup> Tsopano mveterani mwatcheru. Mwamuna kapena mkazi sangakhoze kupita Kumwamba pokhapokha atabadwa mwatsopano. Ine sindikutanthauza chifukwa inu mwayankhula ndi malirime, ine sindikutanthauza chifukwa inu mwafuula, Ine sindikutanthauza chifukwa inu munavina, ine sindikutanthauza chifukwa munapita kutchalitchi ndipo mwakhala kabwerebwere, kuvala mabatani chifukwa cha kukhulupirika kwanu; zinthu zimenezo zonse ndi zabwino, koma izo si Izo. Payenera kukhala mwamtheradi chilumikizano pakati pa inu ndi Khristu, mpaka inu mukhale mmodzi. Ndinu mmodzi! Ndipo ngati inu simuli, bwanji . . . ?

<sup>77</sup> Kodi inu mungalingalire kubwera pa nthawi ya usiku, wotopa, wothodwa, wolema? Ngati ndinu mlimi, makaniko, mlaliki, chirichonse chimene inu muli, mubwera mkati, pamene inu mulowa mnyumba yanu yaying'ono, mukulakalaka mpaka inu mutakhoza kufika kumeneko. Inu nkutsegula chitseko ndipo mkazi wamng'ono wokoma atayima pamenepo, iye nakupatsani inu moni. Iye ali yense atadzikongoletsa ndipo atadzisambitsa. Iye akuyenda ndikukupsyosyonani inu pa tsaya, iye anati, "Adad, inu mwatopa." Iye nkukukhazikani inu pansu pampando, iye nkudzikhazika yekha pamiyendo yanu, iye nkudzayika manja ake mokukumbatirani inu nkumakusisitani inu. Izo zimangowoneka ngati ndiye kuti inu simunatope, chinachake chimakunyamulani inu. Ndi chinachake chimene Mulungu anakupatsani inu kwa cholinga chimenecho. Ndi gawo la inu, tsopano, ngati iye ali mkazi wona.

<sup>78</sup> Koma bwanji ngati milomo imeneyo yapsompsona mwamuna wina tsiku limenero kapena nthawi ina? Bwanji ngati iwe ukudziwa zimenezo? Bwanji ngati mikono imeneyo yakumbatira mwamuna wina? Iye ndi chonyansa mwamtheradi pa miyendo yako. Kupsompsona kumeneko kumayaka ngati kupsompsona kwa Yudasi. Mikono imeneyo, mungafune kuti iyo isakhale mokuzungulirani inu. O, iye akhoza kukhala wokongola, tsitsi lake likhoza kukhala lopiringizika, maso ake akhoza kukhala a bulauni, masaya ake akhoza kukhala ofewa, siketi yake yaying'ono ikhoza kukhala yositidwa, iye akhoza kukhala wokongola kwambiri, koma ngati ulemu weniweni waumulungu umenewo ndi chikondi ndi chidaliro sichiri pamenepo, iye zingakhale bwino asakhale pa miyendo yako. Iwe sumafuna kanthu kochita naye iye, iye ndi a—ali ndi ngongole kwa inu. Ine sindikusamala momwe iye amadzikongoletsera yekha, iye ndiwolakwabe mpaka iye atatsimikiziridwa kuti ndi weniweni, wokondeka weniweni, osakonda wina koma iwe, osati kupsompsona kwina kuchokera pa milomo yake koma yako, palibe mikono ina ikuyenera kumugwira iye koma yako,

ndipo iwe umadziwa izo. Ndi kumverera kotani, ndi chithonhozo chotani!

<sup>79</sup> Ameneyo ndi mwamuna ndi mkazi, chomwe chiri choyimira cha Khristu ndi Mpingo Wake. Ndipo pamene inu mupita kutchalitchi chanu, inu mutha kukhala ndi mipando yabwino kwambiri mumzindawo, inu mutha kukhala ndi nsanja yapamwamba kwambiri yomwe ilipo mumzindawo, inu mutha kukhala ndi limba labwino kwambiri, inu mutha kuvala bwino kwambiri, inu mukhoza kuyimba ngati mbalame yotsanzira, koma zonse za izo, ngati inu mukupsompona ndi kunyengeka ndi dziko, kupsompona kumeneko pamasaya a Khristu ndi kupsompona kwa Yudasi. Iye samafuna kanthu kochita ndi inu. Iye amayang'ana pa mphete yanu ya chitomero chaukwati ndipo Iye amapeza tabuleti yachotsedwa, Iye amapeza chikondi chapita. Ndi mawonekedwe, Iye amapeza kukhulupirika kwapita. Inu mwachita chiwerewere ndi dziko. Inu mumapita ku zovina ndi maphwando a kwasa-kwasa, ndi kuwonera mapulogalamu onyansa a pa televizion. Inu mukuchita chigololo ndi Khristu, pa Iye, monga kumamutcha Iye Mwamuna wanu.

<sup>80</sup> Baibulo linati, “Inu mumati, ‘Ine ndine wolemera, ine sindisowa kanthu.’” Koma Iye anati, “Inu simukudziwa kuti ndinu wamaliseche, womvetsa chisoni, wakhungu, wosauka, ndipo simudziwa izo.” Ndi nthawi yoti tiyatse kandulo ndi kusesa mnyumba. Kudza kwa Ambuye kuli pafupi.

Tiyeni tiganizire izo kwa mphindi zochepa chabe pamene ife tikuweramitsa mitu yathu. Kodi mutero? Kodi inu mungatembenukire ku limba, mlongo?

<sup>81</sup> Kodi inu mwakhala mukuchita chiyani, mpingo? Chikhalidwe chanu nchotani usikuuno? Pamene dzanja lanu lakwezedwa mmwamba mu kudzipereka kwanu, kodi pali chinachake chakufufuzani inu? Ngati inu mukunyengeka ndi dziko, ngati inu mukuchita zinthu zomwe ndi zolakwika, kupsopsona kwanu. . .

<sup>82</sup> Taganizani za izo, bambo. Bambo, ine ndikufuna ndikufunensi inu chinachake. Ndipo izi zikupita kwa Abiti, nanunso, ndipo Mayi Dona Wamng'ono, kodi inu mungaganize chiyani za bwenzi lanu, ngati iwe ukanadziwa kuti iwe wamuwona iye kunja akupsomponana ndi kupitirira ndi atsikana ena, ndipo iwe unali otomeredwa kwa iye, ndipo iye anabwera nakusisitani inu pa dzanja, ndi kunena, “Wokonedwa, ine ndimakukonda iwe wekha”?

Inu mungati, “Wachinyengo wamng'ono iwe, choka pamaso panga!”

<sup>83</sup> Kodi inu mungatani. . .? Taganizani za izo, Bambo. Ife sitinangotomerana chabe, koma ndife okwatirana. Mpingo wakwatiwa ndi Khristu. Ife ndife Mkazi wa Khristu, tikubala ana. Kodi mungakonde bwanji kubwera kunyumba usiku,

chifukwa cha kudzipereka kwanu kwa mkazi wanu, ndipo iye ali ndi gulu la ana aang'ono, ndipo inu mumapeza tsiku limenero...? Ndipo pamene iye abwera mkati, o, zikhadabo zake zikhoza kukhala zopakidwa utoto (ndiko kuti, ngati inu muli wa chidziko). Inu mukhoza...Iye akhoza kuwoneka wokongola kwambiri, koma inu mukudziwa. Taganizani za izo, m'bale, ngati mkazi ameneyo wakhala akupsompsona amuna ena. Ngati manja amenewo amene akuzungulirani inu, akukuuzani inu kuti amakukondani inu, ndipo inu nkumadziwa kuti ndi a...kuti iye amakondanso ena nayenso, chikondi chake sichoona. Chikondi chake sichoona. Icho sichiri kwa inu, icho ndi cha enanso. Ngati pali mwamuna wina kwa inu, inu mungamuchotse iye pamiyendo yanu. Taganizirani za momwe kumverera kwake kungakhalire. Taganizani za izo, dona, ngati mwamuna wanu abwera kunyumba. Osati zokhazo, komanso kunyamula matenda a makhalidwe oyipa.

<sup>84</sup> Ndipo, o, adalitse mtima wanu, mpingo ukudyedwa ndi matenda auzimu, a mitundu yonse ya timalingaliro ndi china chirichonse. Ndizo zolakwika! Mulungu, khalani wachifundo! Yesu akubwera, abwenzi. Inu simukhala nayo nthawi umodzi wa mausiku awa, kapena limodzi la masiku awa. Inu kulibwino mufufuze tspano.

Tiyeni tipemphere:

<sup>85</sup> Ndi angati a inu mukuti, "M'bale Branham," ndi mitu yanu yoweramitsidwa, manja anu atakwezedwa, "mundikumbukire ine mu pemphero lanu, M'bale Branham. Ine ndabwera usikuuno, ine sindinabwere kuno kuti ndidzangowonedwa?" Mulungu akudalitseni inu. Tangoyang'anani pa manjowo. "Ine sindinabwere kuno kuti ndidzawonedwe, ine ndinabwera kuti ndidzapeze chinachake. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Mulungu wayankhula kwa mtima wanga pamene inu mukulalikira, ndipo ine ndikuzindikira kuti ine ndikulakwitsa. Ine—ine ndikufuna kukhala Mkristu weniweni, wona. Ine ndikufuna kukhala wokonda weniweni, kuti pamene ine ndipita kwa Ambuye wanga ndi kugwada pa mawondo anga, Ine ndikufuna Iye kuti adzindikumbatira ine mmikono Mwake, nati, 'O, wokonedwa wanga!'"

<sup>86</sup> Inu mukukumbukira Solomoni, momwe iye anayankhulira za izo? Iye anati, "Bwera, wokonedwa wanga, ife tiyende pakati pa makangaza, ife tiyende m'munda wa zonunkhira." Momwe iye anati milomo yake inkawoneka ngati masamba a rozi, ndi zina zotero. Momwe iye amamukondera mkazi wake wamng'onoyo, anati, "Bwera, tiye ife tipite ndi kukadzazitsa chikondi chathu."

<sup>87</sup> Pamene inu mufika pa guwa lanu kuti mupemphere, kodi mtima wanu ndi wona ndipo moyo wanu ndi wosayipitsidwa mwakuti inu mumati, "Ambuye Mulungu, mulole ife titenge

chikondi chathu,” ndipo inu mukuti, “Inde, Wokonedwa wanga, Ine ndimakukondani Inu”? Kapena, kodi inu mwakhala mukuchita chiwerewere? Kodi inu mwakhala mukunyengeka ndi dziko?

<sup>88</sup> Ndipo ora la Ambuye liri pafupi pamene zizindikiro zonse izi ndi zodabwitsa, ndi ma teni a masauzande a zinthu zina zomwe zachitika, zikuloza, cholemba chirichonse chikuloza. Kukuda. Muli kuzizira mu mpingo. Chitsitsimutso chikuwoneka kuti chatha. Kachidutswa komaliza katsala pang’ono kutha. Ndipo apa ife tikudzipeza tokha mu chigololo. Kodi Iye adzachita chiyani? Iye adzaticankhira ife kuchoka pa miyendo Yake, ndi kunena, “Chokani kwa Ine, inu ochita kusayeruzika.”

<sup>89</sup> Tsopano, ngati pali winawake pano amene akufuna kuti akumbukiridwense kachiwiri, Ine ndikhoza kufunsa pa miniti iyi, kwezani manja anu kwa Mulungu, nenani, “Tsopano ine ndikudzipereka ndi kunena, mwa chisomo cha Mulungu, kuyambira usikuuno mpakana ine ndikhala moyo wona mothandizidwa ndi Mulungu.” Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Ndipo inu m’bale, inu mlongo, inu dona wamng’ono, inu bwana, inu m’bale, inu cha kuno, kumusi uko, ndi inu mnyamata wamng’ono.

<sup>90</sup> Kodi alipo munthu pano amene sanayambe wapulumutsidwapo, ndipo akuti, “M’bale Branham, ndikumbukireni ine, ine sindinayambe ndabadwanso kachiwiri. Ine ndikudziwa sindiri”? Mvetserani, inu simunapulumsidwe mpaka inu mutabadwanso kachiwiri, inu munangotembenezira nkhope yanu kwa Chinachake; koma pamene inu mumuvomereza Khristu inu mumabadwa mwatsopano. Inu mukuti, “M’bale Branham, ine sindinayambe ndachilandira Icho. Ine ndikudziwa ndine wolakwa. Ine tsopano ndikukweza manja anga, ndi kuti, ‘Inu mundikumbukire ine, nanenso.’ Ine sindinayambe ndapulumsidwapo. Ine sindinayambe—sindinayesere nkomwe kumutumikira Khristu, koma ine ndikufuna kuti ndiyesere izo. Ndipemphereni ine, M’bale Branham.” Kodi inu mungakweze dzanja lanu, winawake muno tsopano? Kodi alipo munthu mmodzi muno amene sanakhalepo konse Mkhristu, mungakonde kukweza dzanja lanu, kunena, “Ndikumbukireni ine, m’bale, mu pemphero”? Mulungu akudalitse iwe, mwana. Winawake akuti, “Ndikumbukireni ine, m’bale”? Mulungu akudalitseni inu, dona. Winawakenso, “Ndikumbukireni ine, m’bale, Ine ndikufuna tsopano kukhulupirira pa Ambuye Yesu ndi kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanga”? Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Ndizo zabwino.

<sup>91</sup> Winawake anandidzudzula ine tsiku lina, akuti, “M’bale Branham, chifukwa chiyani inu mumati, ‘Kwezani dzanja lanu?’” Mvetserani, palibe amene amakhulupirira mu kuyitanira kuguwa kuposa momwe ine ndimachitira. Ine

ndimakhulupirira mu kubwera ku guwa, izo nzabwino, koma izo sizimakupulumutsani inu. Ndi lingaliro lanu, lingaliro lanu la Khristu. Inu mukuti, “Chabwino, ngati ine ndikanayenda kupita ku guwa.” Ndizo zabwino. Koma, abale, kodi inu munazindikira pamene inu mukweza dzanja lanu inu mumaswa lamulo lililonse la sayansi limene liripo? Dzanja lanu, mwa chilengedwe, mwa mphamvu yokokera pansi, limayenera kulendewera pansi. Ngati inu mukweza dzanja lanu, zimasonyeza kuti muli chinthu Chauzimu mwa inu chimene chingathe kunyozza malamulo a chilengedwe, kuti mukweze dzanja lanu kwa Mlengi wanu, Chinachake mumtima mwanu chinapanga chisankho. Mulungu amakuwonani inu mukukweza manja anu mofanana basi monga Iye amakuwonerani inu pa guwa. Ndizo zolondola ndendende. Ngati inu mukutanthauza izo, Mulungu amatanthauza izo nayenso. Koma penyani, mzanga, inu simungakhoze kukhala mwatheka, inu muyenera kutanthauza izo.

Tsopano tiyeni ife tipemphere:

<sup>92</sup> Atate Odala Akumwamba, usikuuno pa kuyamba pa chitsitsimutso ichi, pamene nthawi yathu yasesa tsopano, ndipo yadutsa pang’ono, ine ndikukupemphani Inu kuti mukhale wachifundo kwa anthu awa. Ndipo perekani, Mulungu Wamphamvuzonse, kuti . . . Kuno usikuuno pafupifupi manja twente anakwera mmwamba mnyumbayi, kuti iwo akusowa Khristu. O Mulungu, ndi miyoyo yawo. Mzimu, Mafuta, ali pafupi kutha. Sipadzakhalanso ena ambiri. Pamene dontho lotsiriza lichoka mu chidebe, kapena chotengera, sipadzakhalanso Mafuta ena oyikidwa mu nyali. Iwo akuzindikira kuti iwo ali mu tsiku lotsiriza. Palibe chiyebekezo padziko lapansi kwa ife kunja kwa Khristu. Ine ndikupemphera usikuuno, Ambuye, kuti mwinamwake, mu ulemu wa mphindi ino, ulemu, kuti Inu tsopano mutumiza Mzimu Woyera umene unawapangitsa iwo kukweza manja awo, ndi kuwapulumutsa iwo ku moyo wauchimo. Perekani izi, Atate.

<sup>93</sup> Ndipo mulole msonkhano uwu usanathe, mulole pakhale kwenikweni madazeni a iwo, ambiri akufuula ndi Mzimu Woyera. Mulole umu, mobatizira, angokhala mmodzi pambuyo pa mzake kubatizidwa mu Dzina lofunika la Ambuye wathu Yesu Khristu, pa mmawa wa Isitala, kudzuka ku moyo watsopano. O Atate Wodala Wamuyaya, ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo. Perekani izi, Ambuye. Ndipo tsopano, pa mphindi yomwe ino, mulole lingaliro lawo likhale loona, mulole iwo akulandireni Inu pomwe iwo akhala. Maguwa athu ndi pozungulira padzaza ndi anthu, ndipo ife tikupemphera kuti Inu muwalole anthu awa usikuuno akhale antchito Anu. Mu Dzina la Khristu.

<sup>94</sup> Pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikufuna kuti ndikufunsi inu funso limodzi laulemu. Inu amene munakweza dzanja lanu ndi inu amene mumapemphera,

ine ndikudziwa inu simunakweze dzanja lanu kuti mungowona dzanja lanu likukwera mmwamba. Inu munalikweza ilo chifukwa Chinachake chinakuuzani inu kutero. Ndipo inu mukuti, ndi dzanja lokwezedwa, “M’bale Branham, ine ndikukhulupirira, pamaso pa Mulungu ndi gulu ili, Ine ndikukhulupirira kuti chinachake chachitika mu mtima mwanga usikuuno, kuti kuyambira usiku uno mpakana ine ndikhala munthu wosiyana.” Kodi inu mungakweze dzanja lanu, inu amene munakweza dzanja lanu, mukuti, “Ine ndikukhulupirira”? Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, inu, inu, inu. Ndizo zodabwitsa. Kumbuyo komwe mmbuyo, inde, Ambuye akudalitseni inu.

<sup>95</sup> Winawakenso kwezani dzanja lanu, ndikuti, “Ine ndikukhulupirira pakali pano”? Mulungu akudalitseni inu, m’bale. “Ambuye akundiiza ine usikuuno...” Mulungu akudalitseni inu, dona kumbuyo uko. Mulungu akudalitseni inu, dona wamng’ono cha kuno. “Ambuye akundiiza ine pakali pano kuti chinachake chachitika mu mtima mwanga, ndipo ine ndikukhulupirira ine ndikhala ndi chikondwerero chochuluka kuchokera mu chitsitsimutso ichi kuposa chimene ine ndinayamba ndakhala nacho mmoyo wanga.” Mulungu akudalitseni inu. Chabwino, Mulungu akudalitseni inu, dona wakhala apa. Ine ndimaganiza kuti inali pafupifupi nthawi yakuti inu mukweze dzanja lanu, inunso. Kodi pali winanso akuti, “Ine ndikumverera mosiyana, M’bale Branham, Ine ndikukhulupirira ine ndikutuluka mu tchalitchi muno usikuuno ndi chikumbumtima cha kuyandikira posachedwa kwa Khristu. Ine ndikutuluka kuchokera muno kuti ndikakhale moyo wina. Ine ndiwoti ndikakhale Mkristu, mwa chisomo cha Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu wandiyitana ine”?

<sup>96</sup> Ndipo ngati Iye wakuyitanani inu, ndinu Ake. Siyani kunyengeka, siyani kunyengeka ndi dziko! Bwerani, mukhalireni moyo Iye tsopano. Nenani, “Ine ndilapa machimo anga onse, ndipo tsopano ine ndikumutenga Khristu ngati Mpulumutsi wanga.” Kodi pangakhale wina tisanatseke? Kodi alipo? Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu. Ndizo zabwino. Mulungu akudalitseni inu. Ndizo zabwino. Wokondwa kwambiri kukuwonani inu mukuchita zimenezo. Chabwino.

<sup>97</sup> Kuyamba kwa usiku tsopano, ndi pang’ono...Ife basi sitikufuna kuti tiyike kufinya kwambiri kwa izo, ife tikufuna tituluke mofulumira kotero kuti inu mukhoze kubwerera mawa usiku.

<sup>98</sup> Basi ife tisanatseke, alipo munthu wodwala mungakweze dzanja lanu, mukuti, “Ndipempherereni ine, M’bale Branham”? Chabwino, ndiwo faifi, sikisi, seveni, eyiti, naini, manja teni, leveni, thwelofu, chabwino, tsopano satini, fortini, chabwino, fifitini.

Tiyeni ife tiwerame tsopano:

<sup>99</sup> Atate Odala Akumwamba, Inu mwawawona manja amenewo. Ndipo, o, iwo ali pano pa cholinga. Mwina iwo ndi Akhristu, koma iwo akusowa thandizo Lanu lalikulu. Ndipo ife tikuzindikira, Ambuye, kuti Inu munafuula kudzera mwa Davide, anati, “Osayiwala zabwino Zake zonse Amene amatikhululukira mphulupulu zathu zonse, Amene amachiza matenda athu onse.” Ine ndikupemphera kuti Magazi a Khristu akhale mwamtengo wapatali pa iwo ndipo iwo achiritsidwe, kuti asangalale ndi msonkhano ukubwera uwu. Perekani izi, Ambuye. Kupyolera mu Dzina la Khristu ife tikupempha izi. Amen.

Tiyeni tiyime tsopano, *Tenga Dzina La Yesu Nawe*:

. . . Dzinalo la Yesu nawe,  
Mwana . . .

Tiyeni titembenuke, gwiranani chanza ndi winawake pafupi nanu. Tembenukirani mozungulira, gwiranani chanza.

Lidzakukondweretsa ndi kukutonhoza iwe,  
O, litenge Ilo kulikonse komwe upita.

Dzina Lofunika, (Dzina Lofunika) (O kukoma kwake!)

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba;

Dzina Lofunika, (Dzina Lofunika) O kukoma kwake!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe cha Kumwamba.

Tsopano tiyeni ife mwakachetechete, pamene ife kuyang’ana njira iyi, tiyimbe modekha:

Pa Dzina la Yesu tikugwada,  
Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,  
Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka  
Iye korona,

O, pamene ulendo wathu watha.

Dzina Lofunika, (Lodala Ilo.) O kukoma kwake!

Chiyembekezo cha dziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba;


Dzina Lofunika, (Dzina Lofunika!) O kukoma kwake!

Chiyembekezo cha dziko lapansi ndi chimwemwe cha Kumwamba.

<sup>100</sup> Tsopano yangodutsa pang’ono naini, pafupifupi maminiti seveni kapena eyiti itakwana naini. Mofulumira, inu mukhoza kukafika kunyumba, kubwerera mawa usiku ndipo tidzasangalala ndi madalitso a Mulungu, kusangalala ndi

kupezeka kwanu. Ndipo tsopano ine ndinazindikira pafupifupi thwelofu, manja fortini mmwamba kuti achiritsidwe usikuuno. Ngati izo zifika kuti tikangere odwala ambiri mkati, ife tiitanira basi usiku umodzi kwa msonkhano wa machiritso, mwinamwake Loweruka usiku ndi Lamlungu aponso. Ngati ife tiwona kuti sitingakhoze kuwatenga iwo onse Lamlungu, ife tidzatenga Loweruka usiku. Ife tiwona momwe izo zikhalire.

<sup>101</sup> Tsopano ine—ine ndikupemphera kuti madalitso a Mulungu akhale mozama pa aliyense wa inu, ndipo mulole Iye akhale nanu ndi kukudalitsani inu mpaka ife tikhoze kukumana mawa usiku kachiwiri.

<sup>102</sup> Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano mu mphindi yokha ya pemphero, pamene ine ndikuwafunsa abusa kuti abwere kuno ndi kutibalalitsa mu mawu a pemphero. 



57-0417 Kudza Kwachiwiri Kwa Ambuye  
Branham Tabernacle  
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwana ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)